Achieving Business Excellence Through Standards

CHITSANZO CHA UTUMIKI WA MAKASITOMALA

CHOLINGA
Bungwe la Standards Association of Zimbabwe (SAZ) limatsimikizira kudzipereka kwa ogwira ntchito ndikutsogolera khalidwe lathu popereka chithandizo chabwino kwambiri kuti akwaniritse masomphenya ndi cholinga cha bungweli.

NDIFE NDANI
Bungwe la Standards Association of Zimbabwe (SAZ) ndi bungwe loyang'anila ubwino wakakukonzedwa kwa zinthu mokwanira mudziko lonse. SAZ idakhazikitsidwa muchaka cha 1957 ndipo idakhazikitsidwa mwalamulo muchaka 1960. Bungweli ndi bungwe lopanda phindu lodzipereka kupatsira zintchito zapamwamba komanso zozikidwa pa miyezo kuti lipititse patsogolo mpikisano wa zinthu ndi ntchito za makasitomala ake olemekezeka ndikuteteza madera ndi chilengedwe.
Kudzera mu Chitsanzo chake cha Utumiki kwa Makasitomala, SAZ yadzipereka kutsatira njira zabwino kwambiri, kugwiritsa ntchito ukadaulo woyenera pogwlitsa ntchito makina amasiku ano, ndikusunga miyezo yapamwamba kwambiri yaukatswiri ndi makhalidwe abwino nthawi zonse.
Bungweli limayesetsa kulimbikitsa ubale ndi omwe akukhudzidwa mwa kuyang'anira ndikuwunika nthawi zonse mayankho a makasitomala.

MFUNDO ZATHU ZAPAMWAMBA
- **Umphumphu:** Kuchita bwino ngakhale palibe amene akukuona.
- **Kulemekeza ndikuyika wogula pamwamba:** Kukhala ndi chikhalidwe chomwe chimaphatikizapo kupereka zinthu ndi ntchito zomwe zimakwaniritsa kapena kupitirira zosowa ndi ziyembekezo za makasitomala.
- **Zatsopano:** Timalimbikitsa luso lapadera lomwe timayesetsa kuliyika muzinthu ndi ntchito zathu.
- **Kachitidwe kabwino:** Timaona kuti ntchito yathu ndi yabwino kwambiri, ndipo timayesetsa kupereka zotsatira zabwino kwambiri, mautumiki, ndi zokumana nazo zomwe zimapangitsa kuti ntchito yathu ikhale yopindulitsa.
- **Kukhazikika:** Cholinga chathu ndi kupanga zotsatira zabwino pa chuma, chilengedwe ndi anthu komanso kuonetsetsa kuti bungwe lathu likuyenda bwino komanso limakhala lolimba kwa nthawi yayitali.

BIZINESI YATHU
- Kupanga ndi kufalitsa miyezo (standards) ya dziko la Zimbabwe.
- Kulimbikitsa kumvetsetsa zofunikira pa miyezo popereka maphunziro ozikidwa pa miyezo.
- Kuyesa kwa zinthu zopangira ndi zinthu zopangidwa m'ma laboratories motsatira miyezo yoyenera, kuwunika zida, ndi kuwunika zida kuphatikizapo kuwunika komwe katundu wotumizidwa kunja akupita.
- Kulimbikitsa kugwiritsa ntchito miyezo yofala pogwiritsa ntchito njira zovomerezeka ndi chipani chachitatu.
- Kupereka chithandizo chodziwitsa anthu za miyezo ya dziko, chigawo, ndi mayiko ena padziko lapansi.

KUDZIPERETKA KWATHU
SAZ yadzipereka ku mfundo izi:
- **Kusakondera:** Timasankha zinthu motsatira umboni weniweni popanda kukhudzidwa ndi zinthu zakunja.
- **Luso:** Timaonetsetsa kuti ntchito zathu zonse zimaperekedwa ndi akatswiri aluso kwambiri.
- **Kutseguka:** Timapereka mwayi kwa anthu onse wopeza kapena kuulula zambiri zoyenera, zosakhala zachinsinsi, komanso zapanthawi yake zokhudza ntchito zathu kuti tilimbikitse chidaliro pamsika.
- **Kuyankha pazonse:** Timakonza mauthenga onse nthawi yake, ndikuonetsetsa kuti ntchito zathu zikuyenda bwino mwachangu motsatira njira zathu.
- **Chinsinsi:** Timalemekeza makasitomala onse, timawalemekeza, komanso timasunga chinsinsi mwachilungamo.

CHITSIMIKIZO CHA UTUMIKI WATHU
Kuti tikwaniritse chitsimikizo chathu cha utumiki kwa inu, tadzipereka kukhala ndi antchito aluso, kupanga ndi kusunga chikhalidwe chotseguka chomwe chili chachilungamo komanso choyenera pochita ndi makasitomala athu.
Tadzipereka kupereka chithandizo chabwino kwambiri mwa:
- Kumvetsa zofuna ndi zosowa zanu.
- Kukonza utumiki wathu molingana ndi zosowa zanu.
- Kukuchitirani ulemu, ulemu komanso kusunga chinsinsi ngati pakufunika kutero.
- Kukupatsani chidziwitso chomveka bwino, cholondola komanso choyenera.
- Nthawi yofulumira yogwirira ntchito.

KODI MUNGATITHANDIZE BWANJI?
- Perekani chidziwitso cholondola pa nthawi yonse yolankhulana nafe.
- Perekani ndemanga kuti muwongolere ntchito zomwe timapereka.
- Tidziwitseni za kusintha kulikonse komwe tiyenera kudziwa.
- Sungani kudalirika kwa zizindikiro/ma logo athu powagwiritsa ntchito moyenera kapena kunena za kugwiritsa ntchito zizindikirozi molakwika.

Bwana Wamkulu

31/07/2026

Tsiku

Ngati muli ndi mafunso, madandaulo kapena ndemanga chonde imbani, WhatsApp kapena imelo ku:
Standards Association of Zimbabwe:
1 Northend Close, Borrowdale, Harare, Zimbabwe, Lamiya:+263-24-2885511/2/8, Selefoni: +263 775 183 805
marketing@saz.org.zw, www.saz.org.zw